- Muli ndi ufulu woyenda momasuka m'Malawi. Izi zikutanthauza kuti a polisi sangakumangeni chifukwa chopezeka kapena kuyendayenda pa malo ena ake.
- Muli ndi ufulu opita ku khothi kapena ku mabungwe ena ali onse ngati ufulu wanu waphwanyidwa. A polisi akuyenera kumvetsera ndi kutsekula mlandu ngati mwakawadandaulira china chili chonse.
- Muli ndi ufulu kuti musamangidwe popanda chifukwa kapena kusungidwa popanda mlandu.

Kodi ufulu wanga ndi chiyani ngati ndamangidwa?

Ndi chiyani chimene chikuyenera kuchitika ngati ndamangidwa?

- Mukamangidwa apolisi akuyenera kufotokoza chifukwa chimene akumangirani.
- A polisi akuyenereka kupereka umboni wokwanira kuti mwaphwanya lamulo kupanda apo mukuyenera kumasulidwa.
- A polisi akuyenerekanso kukuuzani kuti muli ndi ufulu wokhala chete. Simungakakamizidwe kuyankhula. Koma ngati a polisi akufunsani dzina ndi komwe mumakhala mukuyenera kuyankha moyenera.
- Apolisi sakuyenera kukuchitirani nkhaza kapena kukuopsyezani munjira ina iliyonse. Apolisi sakuyenera kugwiritsa ntchito mphamvu zosavomerezedwa pokumangani.
- Mzimayi omangidwa akhoza kusechedwa ndi wa polisi wamkazi yekha komanso mwa ulemu. Apolisi sakuyenera kukuvulani zovala pa gulu pokusechani.
- Mukakhala m'manja mwa apolisi muli ndi ufulu olandira chithandizo cha mankhwala ngati mwadwala.
- Muli ndi ufulu oyankhula ndi munthu woyimirira milandu (lawyer) kapena Mlangizi waza Malamulo (Paralegal) mwachinsinsi.
- Mukamangidwa apolisi akuyenera kukuyimbani mlandu ngati ulipo ngati palibe mukuyenra kumasulidwa.

Mfundo yofunika kwambiri: Chifukwa chimene apolisi angakumangireni ndi choti mukawonekere ku khothi kukayankha mlandu basi. Apolisi sakuyenera kukumangani ndi cholinga chokulangani, kukuopyesazani kapena kukuchititsani manyazi mukalakwa.

Kodi ufulu wanga ndi otani mu khothi?

- Muli ndi ufulu oyankhula ndi munthu woyimirira milandu (lawyer).
- Ndinu osalakwa pokhapokha umboni utaperekedwa ndikupezeka kuti mwaphwanya lamulo.
- Muli ndi ufulu oweruzidwa mwachilungamo.
- Ngati mwapezeka olakwa ndipo mukuona kuti mulandu siunayende bwino kapena panali kulakwitsa panthawi yoweruzidwa muli ndi ufulu ochita apilu.

Kodi thandizo ndingalipeze kuti?

DZINA LA BUNGWE	THANDIZO	PHONE
Centre for Human Rights, Education, Advice and Assistance (CHREAA)	A CHREAA akhoza kupereka thandizo lokhudza ufulu ndi malamulo komanso pomwe angakwanitse kukuthandizani ndi Woyimilira Milandu (Lawyer). *A CHREAA akupezeka ku Chitawira mu JHANGO House m'mbali mwa msewu wa Soche pafupi ndi Winners Chapel.*	Foni ya ulere MTL : 80000333 TNM : 331 Airtel: 331
Youth Net and Counselling (YONECO)	Uphungu komanso malangizo. Iwo adzakusonyezani komwe mungathandizidwe moyenera	Foni ya ulere 80001234
Malawi Human Rights Commission (MHRC)	Apezeni ngati ufulu wanu waphwanyidwa.	Lilongwe: (+265) 1 750 900/958/954 Blantyre: (+265) 1 831 953/945

SOUTHERN AFRICA LITIGATION CENTRE

CHREAA

AFRICA REGIONAL GRANT ON HIV

REMOVING LEGAL BARRIERS

Dziwani Za Ufulu Wanu

MCHITIDWE WOYENDAYENDA (SEX WORK) NDI MALAMULO A DZIKO LA MALAWI

Kodi mchitidwe woyendayenda (sex work) ndi chiyani nanga munthu woyendayenda ndi ndani?

Anthu opanga mchitidwe woyendayenda atha kukhala akazi kapena amuna amene amalandira ndalama kapena katundu akagonana ndi munthu. Ntchito yoyendayenda ndi njira yopezera ndalama yomwe imachitika pakati pa anthu awiri omwe agwirizana kuti agonane.

Kodi malamulo a dziko la Malawi akuti chiyani pa nkhani ya mchitidwe woyendayenda?

Kodi kugwira ntchtio yoyendayenda ndi kuphwanya lamulo?

Ntchito yoyendayenda ndi yololedwa pa malamulo a dziko la Malawi, komabe milandu yambiri yokhudzana ndi mchitidwewu imagwiritsidwa ntchito ngati chifukwa chotonzera, kuzunza ndi kumanga anthu oyendayendawa. Pa chifukwa chimenechi, ndi zofunika kwambiri kuti muzidziwa ufulu wanu.

Ndi choletsedwa kupanga kapena kuchita zolauwala pa maso pa anthu. Ndizolakwika kulemba munthu kuti akhale woyendayenda kapena kukhala ndi malo ochitirapo zogonana. Ndi zoletsedwa kukakamiza munthu kukhala woyendayenda kapena kusunga munthu asanavomereze pamalo ochitirapo zogonana.

Ndi malamulo ati omwe amagwiritidwa ntchito molakwika pomanga anthu oyendayenda?

Anthu oyendayenda ali pa chiopsyesezo choti atha kumangidwa molakwika pa zifukwa ngati zotsatirazi:

- Kudalira ndalama zopezeka kuchokera mukuyendayenda
- Kuyendayenda usiku (vakabu)

Kudalira ndalama zochokera mu ntchito yoyendayenda ya munthu wina

Cholinga cha mlandu uwu ndi choteteza anthu oyendayenda kwa anthu omwe amafuna kupeza ndalama pogwiritsa ntchito kuyendeyenda kwa anthu ena kapena kufuna kulipidwa chifukwa choti inu mukugwira ntchito yoyendayenda.

Mlandu uwu siukhudza anthu oyendayenda ayi. Lamulo ili silimaletsa munthu kupeza ndalama kuchokera mukuyendayenda kapena kuthandiza abale ake ndi ndalama zochokera ku ntchitoyi ayi. A polisi **sangamange** munthu chifukwa chopeza ndalama kuchokera mukuyendayenda. A polisi akhoza kumanga munthu ngati ali ndi umboni onse kuti munthuyo amapeza ndalama kudzera mukukakamiza munthu wina kugwira ntchito yoyendayendae.

Kumbukirani: Kugwira ntchito yoyendayenda si mlandu ndipo a polisi sangamange munthu chifukwa chopeza ndalama kuchokera mu ntchitoyi.

Vakabu

Ndi ndani amene angamangidwe chifukwa cha vakabu?

A polisi sakuyenera kukumangani ngati mukuyendayenda m'malo ochezera, kaya mukuoneka ngati mukhoza kusokoneza mwa mtundu wina ulionse. Bwalo la milandu lalikulu posachedwapa lanena kuti uwu si mlandu konse potengera ndi malamulo a dziko lino.

A polisi sakuyenera kukumangani pongokukayikirani kapena chifukwa choti munabapo m'mbuyomu ndipo mulibe chochita chodziwika chopezera ndalama komanso mukuluphera kufotokoza chifukwa chopezekera pa malo omwe mwapezekawo. A khothi ananena kuti uwu si mlandu pokhapokha ngati munthu wapezeka wolakwa kapena akuonetsa khalidwe loyipa lomwe m'mbuyomo anapalamula nalo mlandu. Chifukwa choti ntchito yoyendayenda siyoletsedwa, anthu ogwira ntcito yoyendayenda sakuyenera kumangidwa pa mlandu umenewu.

Kodi nanga nditamangidwa chifukwa choyendayenda kapena kuti vakabu nditani?

A polisi akakumangani, mukuyenera kuwafunsa izi:

a. Akuuzeni zifukwa zokumangirani
b. Akuwonetseni umboni womwe akudalira pokumangani
c. Apolisi akuyenera kukuuzani kuti muli ndi ufulu osalankhula chilichonse akakumangani ndiponso kuti ndinu osakakamizidwa kulankhula chilichonse chokhuzana ndi mlandu wanu.
d. Koma apolisi akakufunsani dzina lanu ndi kumene mukuchokera mutha kuwafotokozera zimenezo
e. akukuti akuuzeni zifukwa zimene akumangirani
f. A polisi sayenera kukuwopsyezani kapena kukuchitani nkhana mwanjira ina iliyonse mukamangidwa
g. Mzimayi womangidwa ayenera kupangidwa chipikisheni pa thupi lake ndi mzimayi wa chipolisi osati mzibambo koma apolisiwo sayenera kukuvulani zovala pokupangani chipikishenichi
h. Muli ndi ufulu wopea loya woti akuthandizeni mukamangidwa
i. Mukamangidwa a polisi amayenera kukudziwitsani za mlandu umene mukuyimbidwa pasathe mphindi makumi anayi zisanu ndi zitatai (sic) chipanda apo akuyenera kukutululutsani mu chitokosicho

(A polisi akuyenera kukhala ndi umboni okwanira kuti mwapalamula mlandu kuti mumangidwe kupanda apo kumangidwa uku ndikosaloledwa ndipo mukuyenera kumasulidwa. A polisi sangamange anthu ambirimbiri m'malo osiyanasiyna pa mlandu umodzi. Munthu aliyense akuyenera kupatsidwa mwayi ofotokoza mbali yake mu khothi malingana ndi mlandu womwe iye wapalamula.

Nthawi zina apolisi amaumiriza anthu ogwira ntcito yoyendayenda kuvomera mlandu, ngakhale kuti anthuwa amakhala asalanalakwe. Simukuyenera kuvomera kuti mwapalamula pamene simunalakwe.

Ngati mukufuna uphungu wa za malamulo uzani a police akupezereni mabungwe kapena anthu ophunzitsa za malamulo kuti akuyankhuleni. Ngati mungathe imbali foni yaulere ku CHREAA kuti muthandizidwe.

Kodi anthu ogwira ntchito yoyendayenda ali ndi ufulu?

Ndi ufulu otani omwe ndili nawo ine monga oyendayenda?

Munthu aliyense ali ndi ufulu potengera malamulo adziko lino. Kugwira ntchito yoyendayenda sikutanthauza kuti inu mwasiya kukhala munthu chotero maufulu onse amene munthu wina aliyense ali nawo inunso muli nawo.

Malamulo a dziko lino amanena kuti akuluakulu a boma, kuphatikizapo apolisi ndi oweruza milandu, akuyenera kelemekeza ndi kuteteza ufulu wa anthu onse kuphatikizapo anthu ogwira ntchito zoyendayenda ndi ena onse.

- A polisi akuyenera kukulemekezani osati kukupatsani chibalo kapena kukuchititsani manyazi chifukwa choti ndinu oyendayenda. Muli ndi ufulu kulemekezedwa ndikusungiridwa chinsinsi.
- Simukuyenera kusalidwa chifukwa cha mtundu wanu, kapena kuti ndinu mkazi kapena mamuna, chiyankhulo, chipembedzo, maganizo anu, dziko lanu, komwe mukuchokera, kupuwala, chuma, chibadwa, ntchito kapena mmene mumadziwikira. Izi zikutanthauza kuti a polisi sakuyenerea kukumangani pa chifukwa chokhacho choti ndinu munthu oyendayenda.
- Ngati mwamangidwa pa chifukwa china chilichonse, simukuyenera kutonzedwa kapena kuzunzidwa munjira ina iliyonse chifukwa choti ndinu oyendayenda ayi. Simungazunzidwe mopitiriza chilango chanu kapena kunyozedwa chifukwa choti ndinu oyendayenda.